Kodi *Ndiyenera* Kuchita Chiyani pa Nkhani ya Mowa?

1

Yerekezani kuti muli paphwando ndipo anzanu ena amsinkhu wosafunika kumwa mowa, apezeka kuti amwa.

Kodi mungatani?

GANIZIRANI IZI

BAIBULO LIMATI: **“Wochenjera ndi amene amati akaona tsoka amabisala, koma anthu osadziwa zinthu amangopitabe ndipo amalangidwa.”—Miyambo 22:3.**

Poganizira mfundo ya palembali, yankhani mafunso ali m’munsiwa.

Kodi chingachitike n’chiyani ngati mutakhalabe paphwandolo?

_____

_____

Kodi mungatani kuti muchokepo mosamala kuti isakhale nkhani yaikulu komanso kuti anzanu asakusekeni?

_____

_____

_____

Kodi mukuona kuti **simungapirire** ngati anzanu atakusekani?

_____

_____

ZIMENE ZINGAKUTHANDIZENI

Mukambirane ndi makolo anu kuti muwaimbira foni kapena kuwatumizira meseji ngati mutaona kuti mukufunika kuchokapo mwamsanga paphwandolo.

Zimene ndingachite ngati nditapita kuphwando linalake ndipo anthu ayamba kuledzera:

_____

_____

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2

Tiyerekezenso kuti munthu wina akukukakamizani kuti mumwe.

Kodi mungatani?

GANIZIRANI IZI

BAIBULO LIMATI: **‘Ngati mukudzipereka kwa winawake . . . mumakhala kapolo wake chifukwa chakuti mumamumvera.’—Aroma 6:16.**

Poganizira mfundo ya palembali, yankhani mafunso ali m’munsiwa.

Mukuganiza kuti chingachitike n’chiyani ngati simungayankhe molimba mtima?

_____

_____

Kodi kusadziderera n’kothandiza bwanji ngati anzanu atakukakamizani kuti muchite zinazake?

_____

_____

_____

ZIMENE ZINGAKUTHANDIZENI

Muzidziwiratu zimene munganene. “Ndimakonda kunena kuti, ‘Ayi. Panopo ayi.’ Ndikatero amandisiya ndipo sandivutitsanso.”—Brianna.

Zimene ndinganene ngati munthu wina atandikakamiza kuti ndimwe mowa:

_____

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3

Munapita kocheza ndi anzanu ndipo mwazindikira kuti mnzanu amene amayendetsa galimoto waledzera.

Kodi mungatani?

GANIZIRANI IZI

BAIBULO LIMATI: **“Munthu woyenda ndi anthu anzeru adzakhala wanzeru, koma wochita zinthu ndi anthu opusa adzapeza mavuto.” —Miyambo 13:20.**

Poganizira mfundo ya palembali, yankhani mafunso ali m’munsiwa.

Mukuganiza kuti chingachitike n’chiyani ngati mutalola kuti dalaivalayo akuyendetsenibe popita kunyumba?

_____

_____

Kodi mungachitenso zotani?

_____

_____

_____

Kodi zimene mungachitezo zingathandize bwanji dalaivalayo komanso anthu ena?

_____

_____

ZIMENE ZINGAKUTHANDIZENI

Pewani kukwera galimoto imene dalaivala wake ndi wokayikitsa. Nthawi zonse muzikonzeratu njira ina imene mungafikire kwanu.

Zimene ndingachite ngati munthu amene akuyendetsa galimoto waledzera:

_____

_____

_____

www.jw.org © 2016 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania